# Lonjezo Lopambana Koposa





**Buku ili limatiuza za lonjezo lopambana koposa onse... ndi zomwe Mulungu anachita pokwaniritsa lonjezolo.**

# Mulungu amakukondani ndipo amakwaniritsa Malonjezo ake.

Mulungu chilengere dziko lapansi,
Analonjeza kukonda ndi kusamalira
anthu a padziko.

Nthawi zina anthu amaswa malonjezo...
koma Mulungu akangolonjeza,
Amakwaniritsa!



# Anthu amaswa malonjezo awo pochita zinthu zolakwika:

- Amaiwala za Mulungu.
- Samvera Mulungu.
- Amapwetekana wina ndi mnzake.

**Mulungu akunena kuti chilango chathu pochita zinthu zolakwika zimenezi ndi choti sitingakhale naye limodzi.**

---

**Tchimo:** Liu la m'Baibulo losonyeza za kuganiza, kulankhula kapena kuchita zinthu zomwe Mulungu wati tisachite.

**"Pakuti onse anachimwa (Kuchita zinthu zoipa) Naperewera mu ufumu wa Mulungu"**
**(Aroma 3:23)**



# Mulungu anakwaniritsa lonjezo lake potumiza Yesu.

**Mulungu sanaswepo lonjezo lake la kukonda anthu. Anakonda anthu kwambiri kotero anatumiza mwana wake Yesu kuti adzakhale ndi anthu ndi kuonetsa chikondi cha Mulungu.**

**Yesu anabwera ngati mwana wakhanda,
ndipo anthu ochepa okha
anazindikira kuti Iye anali ndani...
Mwana m'modzi yekhayo
wa Mulungu, Mpulumutsi.**

**Mpulumutsi:** Yesu, yekhayo amene angathe kupulumutsa kapena kuwombola ena ku zinthu zoipa zomwe amaganiza, Ndi kulankhula ndi kuchita: tchimo lawo.

**"Mulungu adaonetsa chikondi chake kwa ife: Anatumiza Mwana wake m'modzi yekha pa dziko lapansi."
(1 Yohane 4:9)**



Yesu anakula nakhala bambo.
Analankhula za Mulungu, Atate Ake,
kwa aliyense amene anakomana naye.

Yesu adauza anthu za lonjezo la Mulungu loti amawakonda.

Yesu anawaonetsa anthu
za momwe angankondere Mulungu ndi
momwe angakonderane wina ndi mnzake.

**Ndipo masiku onse anali**
**ndi nthawi yocheza ndi ana!**

"Koma Yesu anawaitana ophunzira ake nati, 'Alekeni anawa azibwera kwa Ine, musawaletse.'"
(Luka 18:16)



Koma anthu ambiri sanamkonde Mulungu,
kotero anamupha Yesu.

Yesu analolera kuti amchitire zimenezi
chifukwa amatenga chilango
cha zoipa zonse zomwe aliyense anazichita.

## Yesu anafa.

Yesu anafa kuti anthu onse—
anthu monga inu ndi ine—
tikakhulukidwe chifukwa cha zoipa ndi kukakhala ndi
ubwenzi ndi Mulungu tsopano ndi kunthawi yamuyaya.

**Yesu anakuferani chifukwa Amakukondani**

---

**Kukhululukira:** kupanga chisankho choti usiye chilango chomwe umafuna kupereka chifukwa cha maganizo.
**Kudalira:** kuika mtima kapena kukhulupirira chinthu; kuchitapo kanthu pa zomwe umakhulupirira.

**"Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero kuti anatumiza mwana wake wobadwa yekha kuti yense wokhulupirira Iye asataike koma akhale nawo moyo wosatha."**
**(Yohane 3:16)**



Lonjezo la Mulungu silinathe pamene Yesu anafa.
**Gawo lopambana kwambiri linali kubwerabe!**

Mulungu anamuukitsa Yesu nakhala ndi moyo.
Anthu ambiri anamuona nalankhula naye.

## Yesu anakhalanso moyo

kuti aonetse kuti Iye ndi Mulungu
Ali ndi mphamvu zothandizira
iwe kuti uleke kuchita zoipa
ndi kukhala monga momwe
Mulungu akufunira.

"Koma Ine ndabwera kuti mukhale ndi moyo ndipo moyo wake wochuluka."
(Yohane 10:10)



Yesu anabwerera kukakhala ndi Mulungu.

Yesu asanachoke, analonjezanso...

- Yesu akulonjeza kuti akhala nanu ngakhale simungathe kumuona.
- Yesu akulonjeza kukhala nzanu wapamtima.
- Yesu akulonjeza kuti akukhululukirani zoipa zonse zomwe mwakhala mukuchita.
- Yesu akulonjeza kukhala mwa inu ...pamene mukonda kapena kudana ...pamene musangalala kapena kukhumudwa.
- Yesu akulonjeza kuti mukadzafa mudzakhala naye mpaka muyaya.

Mungakonde kupempha Yesu kuti akhale nanu ndi kukhala mwa inu tsopano?

"Ineyo ndili nanu masiku onse."
(Mateyo 28:20)

"Sindidzakusiyani konse."
(Ahebri 13:5)



# Lankhulani ndi Mulungu...

pogwiritsa ntchito mau anu kapena pemphero monga ili:

"Wokondeka Mulungu, ndikukhulupirira kuti
Yesu ndi Mwana wanu.
Zikomo kuti Yesu anafa pamtanda chifukwa cha zoipa
zanga zomwe ndakhala ndikuchita.
Chonde ndikhululukireni chifukwa chochita zoipa.
Ndikupempha kuti Yesu akhale nane ndi kukhala
mwa ine nthawi zonse.
Ndithandizeni kuti ndikhale momwe Inu mukufunira.
Zikomo poyankha pemphero langa."

**Mungakonde kupemphera pemphero limeneli tsopano?**
Dalirani malonjezo a Mulungu kuti amakukondani ndinso kuti Yesu akhala nanu.

"Onse (azibambo, azimai, anyamata, atsikana) amene adaamlandira namkhulupirira Iye, anawapatsa mphamvu zoti akhale ana a Mulungu."
(Yohane 1:12)

**Pemphero:** Kulankhula ndi Mulungu mokweza mau kapena mwakachetechete.



Pamene mupempha Mulungu kuti akukhululukireni
ndi kuitana Yesu kuti akhale nanu...
**Iye alidi ndi inu ndiponso mwa inu**
—lero ndi kunthawi zonse.

Simungamuone Yesu,
ndipo mwina simungaone kusinthika kulikonse.
Koma zoonadi Yesu ali nanu!
Analonjeza kuti adzakhala nanu...
ndipo nthawi zonse amasunga malonjezo ake.

Tsiku ndi tsiku, muyamikeni Yesu
chifukwa chokhala nanu,
ndinso chifukwa chokuthandizani
pa moyo wanu ndi Iye.

---

**Chikhulupiriro** ndi kukhulupirira zinthu zomwe sitingazimvetse; kudalira malonjezo a Mulungu...ndi Mwana wa Mulungu... osatengera ndi momwe mukumvera.

"Nonsenu ndinu ana a Mulungu chifukwa mumakhulupirira Khristu Yesu."
(Agalatiya 3:26)



Ngakhale mutampempha Yesu kuti akhale mwa inu, zikhonza kutheka kuti simukhala achifundo kwa anzanu,
kapena kunena bodza,
kapena kusamvera,
kapena kukhala ndi malingaliro odzikonda.

Nthawi iliyonse mukachita kanthu komwe mukudziwa kuti nkolakwika, muuzeni Mulungu.
Vomerezani ndi Iye kuti zomwe mwachitazo kapena kuganizirazo si zomwe Iye amafuna kuti muchite.

Yamikani Mulungu chifukwa chokukhululukirani.

---

**Kuvomereza:** kunena zoona za momwe Mulungu alili; kuuza Mulungu kuti mukuvomereza kuti zomwe mwaganiza mwanena, kapena mwachita sizinali

"Ngati tivomereza machimo athu Mulungu ndi wokhulupirika ndi wolungama kukatikhululukira ndi kutiyeresa kutichosera chosalungama chilichonse." (1 Yohane 1:9)

**Mulungu wapanganso malonjezo ena odabwitsa.** Iye walonjeza kuti akuthandizani kuti mukule m'moyo wanu watsopano ndi Yesu.



Mukhonza kuyamba kudziwa malonjezo a Mulungu...
...powerenga mavesi a m'Baibulo mkabuku aka.
...popita ku malo komwe anthu amaphunzitsa za Yesu.
...polankhula naye tsiku ndi tsiku.

Mukhonza kuwuza anzanu kapena abanja lanu zomwe mwaphunzira zokhudza Yesu.
Mukhonza kuwawerengera buku ili ndi kuwathandiza kuti apemphe Mulungu awakhululukire.
Ndi thandizo lanu akhonza kupempha Yesu kuti akhale nawo ndi kukhala mwa iwo.


Nthawi zonse,
**dalirani malonjezo a Mulungu...**
**Amachita zomwe wanena.**

**Lonjezo langa...**

Lero, pamene ndapempha, Mulungu wandikhululukira zoipa zonse zomwe ndinazichita ndi kuziganiza. Tsopano Yesu ali nane ndipo ali mwa ine. Ndikufuna kukhala munthu amene Mulungu akufuna kuti ndikakhale. Ndikufuna ndikule ndikukonda Mulungu pamodzi ndi anthu ena.

Dzina langa: ______________________

Tsiku: ______________________



Written by Vernie Schorr

**Chichewa**

©1990 The JESUS Film Project
Reprinted by Foursquare Missions Press with permission.

Bible verses in this book worded for ease of understanding.

Pictures in this booklet used by permission of The JESUS Film Project and taken from "JESUS," a 2-hour film on the life of Christ. For more information on "The Story of Jesus for Children" video or additional material, contact: The Story of Jesus for Children, 910 Calle Negocio, Ste. 160, San Clemente, CA 92673, USA, 1-800-432-1997, www.jesusforchildren.org